
# *CHICHEWA Heart Book*

## Mtima vva Munthu



Copyright: ANGP

**COPYRIGHT:**

**ISBN 0 - 908412 - 01 - 0**

**E-MAIL: info@angp.co.za**
**ALL NATIONS GOSPEL PUBLISHERS**
**Posbus 2191, PRETORIA, 0001, R.S.A.**

(A Gospel Literature Mission financed by donations)
(Reg. No. 1961/001798/08)

**THE HEART OF MAN**

**OR**

**THE SPIRITUAL HEART MIRROR**

(An Allegorical Representation in Ten Pictures)

This booklet originated in France in 1732, was revised and rewritten for the mission fields of Africa by Rev. J.R. Gschwend in 1929, and has subsequently been translated and printed under copyright in over 538 indigenous languages by All Nations Gospel Publishers who are distributing it today in 127 mission countries. People of all languages, classes and religions are being led by this booklet to experience the deep spiritual truth and significance of God's message to mankind as expressed by the prophet Ezekiel 586 years before Christ, "I will give you a new heart and a new mind then you will be my people, and I will be your God!" Ezekiel 36:26-28.

Yense wakucita cimo, acitanso kusayeruzika;ndipo cimo ndilo kusayeruzika.

Ndipo mudziwa kuti lyeyu anaonekera kudzacotsa macimo, ndipo mwa lye mulibe cimo.

Yense wakukhala mwa lye sacimwa; yense wakucimwa samuona lye, ndipo sanadziwa lye.

Tiana, munthu asasokeretse inu; iye wakucita colungama ali wolungama, monga lyeyu ali wolui'lgama.

lye wocita cimo ali wocokera mwa mdierekezi, cifukwa mdierekezi amacimwa kuyambira pa ciyambi. Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndipo kuti akaononge nchito za mdierekezi.

Yense wobadwa kucokera mwa Mulungu sacita cimo, cifukwa ndeu yace ikhafa mwa lye; ndlpo sakhoza kucimwa, popeza wabadwa kucokera mwa Mulungu.

Mmenemo aoneka ana a Mufungu, ndi ana a mdierekezi, yense wosacita cifungamo si afi wocokera mwa Mufungu; ndi iye wosakonda m'bale wace.

1 Yohane 3:4-10.

Mtima vva Munthu

Kacisi wa Mulungu kapenamogwiramo nchito Satana.

(1 Yohane 3:4-10)

Pamene muwerenga buku limeneli kumbukirani kuti liri ngati kalilole m'mene mungathe kudzionera nokha. Ngakhale muli akunja, kapena Akristu, kapena osakhulupirira, kapena obwerera, mudzaona nokha, monga Mulungu amaonera inu. Pakuti Yehova saona monga aona munthu. 1 Samueli 16:7. Mulungu alibe tsankhu.

Satana ndi atate wa anthu onse abodza. lye ali mfumu ya mdima ndi mulungu wa dziko lapansi, amene amadzisandutsa mngelo wa kuunika kuti anyenge amuna ndi akazi. Masiku ano ngakhalenso masiku akale aphunzitsi onyenga amadziyesa okha kuti ali atumiki a Kristu. Ndiponso palibe, kudabwa,. cifukwa satana mwini wace adzionetsera yekha ngati mngelo wa kuunika (2 Akorinto 11 :13, 14). Satana, mulungu wa dziko lino lapansi, aphimba maso ndi maganizo a anthu kuti sangathe kuona kuti Mulungu awakonda iwo kapena kuti Yesu Kristu anafa kupulumutsa iwo. Onse ocimwa ndi osakhulupirira ali akufa ndi akhungu pa za Mulungu. Alikulamulidwa ndi mzimu wa mulungu wa pansi pano (Aefeso 2:2). Ngati maso atseguka adzaona kuti alikupita ku ciononngeko. lye amene anena, "Ndilibe ucimo" adzinyenga yekha "Potero mverani Mulungu; koma kanizani mdierekezi, ndipo adzakuthawani inu. Yandikirani kwa Mulungu, ndipo adzayandikira kwa · inu. Sambani manja, ocimwa inu; yeretsani mitima, a mitima iwiri inu". Yakobo 4:7,8.

Pamene muwerenga bukuli ndi kuphunzira zithunzi-thunzi zace, mudzatha kuona m'kati mwa mtima wanu. Lolani ciyero oa Mulungu kukuonetsani inu makhalidwe a mtima wanu. Ngati mupeza mtima wanu uli woipa, musakane macimo anu koma kuwabvomereza, pakuti Mau a Mulungu atiuza ife kuti "Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi. Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama lye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. Tikanena kuti sitidacimwa, timuyesa lye wonama, ndipo mau ace sakhala mwa ife" (1 Yohane 1 :1-10). "Mwazi wa Yesu Kristu, Mwana wa Mulungu, utisambitsa kuticotsera ife kucosalungama ciri conse".

Muli wolamulidwa ndi Mulungu kapena Satana. Muli kapolo wa ucimo kapena kapolo wa Mulungu. Ngati ucimo ulamulira moyo wanu, musaukane ai, koma pfuulani kwa Mulungu. lye adzakumasulani kupyolera mwa Yesu Kristu amene anadza m'dziko lapansi kuombola ocimwa ndi kutsegula maso a

Copyright: ANGP

mdima ndi kuthyola mphamvu ya Satana ndi ucimo uli mwa ife. Iye ali ciombolo cathu. Mulikuimirira pamaso pa Mulungu Woyera amene amaona maganizo obisika ndi zocita za moyo wanu. Simungakhoze kudzibisa pamaso pa Mulungu, pakuti "Kodi Iye wakupanga khutu ngwosamva? Kodi Iye wakuumba diso, ngwosapenya?" (Masalmo 94:9).

"Pakuti maso a Yehova ayang'ana uko ndi uko m'dziko lonse lapansi, kudzionetsera wamphamvu kwa iwo amene mtima wao uli wangwiro ndi Iye" (2 Mbiri 16:9).

"Pakuti maso ace ali pa njira ya munthu ali yense, napenya moponda mwace monse. Palibe mdima kapena m'thunzi wa imfa, kuti ocita zopanda pace abisaleko" (Yobu 34:21-22).

"Koma Yesu sanakhulupirira iwo kuti akhale nao, cifukwa Iye anadziwa anthu onse". (Yohane 2:24).

Ncifukwa cace "Wodala munthuyo wokhululukidwa cimo lace; cokwiriridwa coipa cace. Wodala munthuyo Yehova samuwelengela mphulupulu zace; ndipo mumzimu mwace mulibe cinyengo" (Masalmo 32:1-5). (Werengani Masalmo 51). Yesu alikuitanabe lero: "Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu" (Mateyu 11:28-30).

Copyright: ANGP

## 1 KAFOTOKOZEREDWE KA ZITHUNZI - THUNZI CITHUNZI COYAMBA



Cithunzi ici cirikuonetsa mtima wa munthu wakunja umene unafotokozedwa m'Buku Lopatulika monga wocimwa mmodzi wolamulidwa ndi mzimu wa dziko lino ndi zofuna zace za thupi. lei ndi cithunzi coona ca mtima monga m'mene Yehova ationela. Maso ace ofiira alikuonetsa kuti ndi woledzera, monga timawerenga m'buku la Miyambo 23:29-32. "Ndani afiira maso? Ndi amene acedwa pali vinyo, napita kukafuna-funa vinyo wosanqanizidwa. Usayang'ana pa vinyo alikufiira. Alikung'azimira m'cikho. Namweka mosalala. Pa citsiriziro cace aluma ngati njoka, najumpha ngati mamba. Maso ako adzaona zacilendo; mtima wako udzalankhula zokhota".

Pansi pa mutu m'cithunzici mtima wa munthu uwonekera-mokhalamo nyama za mitundu-mitundu zimene zikhala chitsanzo ca macimo a mitundu-mitundu mu mtima mwa munthu, monga mtima uli cipinda ca macimo athu. Mulungu atiuza za mneneri Yeremiya kuti: "Mtima ndiwo wonyenga koposa, ndi wosaciritsika, ndani angathe kuudziwa?" (Yeremiya 17:9). Yesu mwini wace anakhazikitsa ici mwakunena kuti:

"Pakuti m'kati mwace mwa mitima ya anthu, mutuluka maganizo oipa, cinyengo, manyozo, diso loipa, mwano, kudzikuza, kupusa: zoipa izi zonse zituluka m'kati, nizidetsa munthu" (Marko 7:21-23).

1. NTHIWATIWA.-Monga munthu ali yense amakhumbira kukongola kwace kwa nthiwatiwa, pano m'kati mwa mtima wa munthu, ikusonyeza za chime la kunyada. Lusifala anali mngelo wamkuru wa Mulungu ndipo anagwa cifukwa ca kunyada kwace nakhala mdani wa Mulungu (Yesaya 14:9-17; Ezekieli 28:12-17).

Kunyada kumacokera ku gahena ndipo kumaonetsa njira zambiri. Ena amadzitama cifukwa ca cuma cao, ng'ombe zao, nkhosa zao, nyumba kapena dziko limene ali nalo, zobvala zao za mtengo wapatali, kukongola kwa nkhope ndi thupi lao. Ena amadzitama cifukwa ca mtundu wao, cifukwa ca kuphunzira kwao kwapamwamba, mphamvu za m'thupi ndi zimene apindula nazo pa dziko lino lapansi. Ena a mayesa kudzikongoletsa · ndi kubvala mkanda, mphete, kapena kutema mphini nkhope ndi matupi ao. "Mulungu akaniza odzikuza koma apatsa cisomo kwa odzicepetsa" (1 Petro 5:5). Kunyada ndi

kudzikuza Mulungu amadana nako (Miyambo 8:13). "Kunyada kutsogolera ku ciononngeko; mtima wodzikuza ndi kutsogolera kupunthwa" (Miyambo 16:18).

2. TONDE.-Tonde amasonyeza ucimo wa zilakolako za thupi ndi cigololo ndi ciwerewere. Macimo ochulidwa pamwambawa aonjezedwa masiku ano kotero kuti tibvomereza coonadi ca mau aYesu pamene lye ananena, pafupi-fupi zaka zikwi ziwiri (2 000) zapitazi, kuti m'masiku otsiriza adzanga ngati masiku a Soclomo ndi Gomora. Mzimu wa masiku · ano wagwira mitima ya anthu oyera ndipo walowa mnjira zosiyana-siyana mobisika. Mbeu yoipa imadzalidwa mu· mtima mwakupyolera kanema, malemba oipa, camba coipa, ndi zina zotere. Cimene Mulungu acicha ucimo m'Buku Lopatulika n'cimene anthu acicha cabwino masiko ano. Anthu salikutsata cltsanzo ca anthu oyera monga Yosefe (Genesis 39). ndi ena koma amatsata citsanzo ca anthu

oipa.Anthu a mtundu wa ci Zulu, cimoclzimoclzinso wa ci Sutu, ndi mitundu yina, amamucha "garu" munthu amene acita cigololo. Munthu wotereyu sadzaona fumu wa Mulungu, "Pakuti kunja kuli agaru ndi anyanga, ndi acigololo, ndi ambanda, ndi opembedza mafano, ndi yense wakukonda boclza ndi kulicita" (Cibv. 22:15). Mulungu atiuza ife kusasewera ndi ciwerewere koma tithawe ico. "Cimo liri lonse munthu akalicita liri kunja kwa thupi; koma waciwerewere acimwira thupi lace la iye yekha. Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo · simukhala a inu nokha" (1 Akorinto 6:15-20). "Ngati wina aononga kacisi wa Mulungu, ameneyo Mulungu adzamuononga, pakuti kacisi wa Mulungu ali wopatulika, ameneyo ndi inu" (1 Akorinto 3:17).

3. NKHUMBA.-Imasonyeza ucimo wakuledzera ndi dyera ndi kususuka. Nkhumba njauchisi, imadya zinthu zonse, sisankhula kanthu pakati pa cinthu cabwino ndi coipa. Iri ngati anthu amene amadya nyama yakufa yokha cifukwa camatenda kapena imene yagwiridwa pa khosi. Amadya mwazi, mbewa ndi makoswe, ndi zina, zimene Mulungu anati tisadye (Macitidwe 15:20; Yesaya66:3-7).

Mwa njira yomweyo mtima wocimwa umadya maganizo oipa, zonena zoipa, zithunzi-thunzi zoipa, malemba oipa, ndi zina zotere. Thupi linalengedwa kukhala kacisi wa Mulungu wamoyo, ladetsedwa ndi cakudya coipa ndi kudya fodya, camba ndi mankhwala ena akupha. M'khatidwe wakusuta todya ngakhale "camba" zaipitsa amuna ngakhale akazi kusiyana ndi kale ndiye Satana amene amamanga anthu m'macimo akusuta fodya. Koma mphamvu ya Mulungu yekha ingakhoze kuwamasula m'macimo aukapolo wa Satana. Anthu ochedwa akristu akalowa m'chalichi sasuta fodya cifukwa amaopa kuipitsa kacisi wa Mulungu. Koma akatuluka kunja amasuta, aiwala kuti kacisi wa Mulungu ndi thupi lao. "Kodi simudziwa kuti muli kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu? Ngati wina aononga kacisi wa Mulungu, ameneyo Mulungu adzamuononga; pakuti kacisi wa Mulungu ali wopatulika, ameneyo ndi inu" (1 Akorinto 3:16-17). "Thawani dama. Cimo liri lonse munthu akalicita liri kunja kwa thupi; koma waciwerewere acimwira thupi lace la iye yekha. Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri Kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha" (1 Akorinto 6:18-19).

Munthu wadyera aliwoipa pamaso pa Mulungu. Timadya kuti tikhale ndimoyo; sitikhala ndi moyo kuti tidzidya ai. Njala in-gathe kukhutitsidwa ndi cakudya cabwino. Koma cilakolako cidzafuula nthawi zonse, "Patseni, patseni!"

Cilakolako sicidzakwaniritsidwa. Monga cilamulo ca m'Cipangano Cakale munthu wadyela ndi woledzera, analikuponyedwa miyala nafa (Deuteronomo 21 :18-21 ). "Pakuti wakumwaimwa ndi wosusukayo adzasauka; ndipo kusinza kudzabveka munthu nsanza. Wosunga cilamulo ndiye mwana

Copyright: ANGP

wozindikira" (Miyambo 23:21; 28:7). Kumbukirani kuti munthu wina wolemera, wodyela ndi kapopolo pa zolaka-laka zace anafa ndipo pamene anali m'gahena anamva zowawa zazikulu. Kuipa kwace kwa kumwa sikufunika kuchulidwa. Pakuti onse adziwa kuti Mulungu atiuza ife mwacimvekere m'mau ace kuti palibe oledzera adzaona Ufumu wa Mulungu. Mowa sicakudya al, ncakumwa caukali cimene cimasokoneza maganizo, kotero kuti kwa iwo amene akumwa amacita mwa ucitsiru. Amakhala oipa ndipo angathe kuphana wina ndi mnzace cimene mwina iwo sakadacicita. "Vinyo acita ciphwere, cakumwa caukali clsokosa; wosocera nazo alibe nzeru" (Miyambo 20:1 ). lwo amene apanga ndi kugulitsa cakumwa caukali ali ocimwa pamaso pa Mulungu, pakuti Mulungu akuti "Tsoka kwa iwo amene ali a mphamvu yakumwa vinyo, ndi anthu olimba akusanganiza zakumwa zaukali" (Yesaya 5:22). "Tsoka wakuninkha mzace cakumwa, ndi kuonjezako mankhwala iko, ndi kumledzeretsa, kuti upenyerere manyazi ao!" (Habakuku 2:15). "Ndipo zeze ndi mgoli, ndi lingaka ndi citoliro, ndi vinyo, ziri m'maphwando ao; koma iwo sapenyetsa nchito ya Yehova" (Yesaya 5:12). "Musasoceretsedwe. Adama, kapena opembedza mafano, kapena olanda, kapena acigololo, sadzalowa Ufumu wa Mulungu" (1 Akorinto 6:9,10).

Macimo acibadwidwe cathu aonekera, ndiwo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsya mtima, zotetena, magawano, mipatuko, njiru kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; iwo akucita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu (Agalatiya 5:19-21). "Ndipo musaledzere naye vinyo, m'mene muli citayiko; komatu mudzale naye Mzimu" (Aefeso 5:18).

Ngati muli ndi ludzu Yesu alikukuitanani: "Ngati pali munthu akumva ludzu, adze kwa Ine, namwe" (Yohane 7:37,38). "Inu nonse, inu akumva ludzu, idzani kumadzi: ndi osowa ndarama idzani inu mugule mudye; inde idzani, mugule vinyo ndi mkaka opanda ndarama ndi opanda mtengo wace" (Yesaya 55:1). "Koma iye wakumwa madzl amene Ine ndidzampatsa sadzamva ludzu nthawi zonse; koma madzi amene Ine ndidzampatsa adzakhala mwa iye kasupe wa madzi otumphukira ku moyo wosatha" (Yohane 4:14).

4. FULU. (Tortoise) Asonyeza za ucimo wa ulesi, kuzengereza ndi nyanga. Kusakhulupirira kuli ngati ucimo wakucita nyanga. "Cifuniro ca waulesi cimupha; cifukwa manja ace akana kugwira nchito. Ena asirira modukidwa tsiku lonse" (Miyambo 21 :25,26). Yoswa ananena mau awa kwa ana Israeli, "Musakhale aulesi pakupindula za m'nthaka". M'khalidwe wa munthu uli waulesi pakufuna zinthu za Mulungu. Yesu anati, "Yesetsani kulowa pa khomo lopapatiza" (Luka 13:24). "lye amene afuna adzapeza". "Ufumu wa Kumwamba uli wokangamizidwa, ndipo wokangamirawo aukwatura ndi mphamvu" (Mateyu 1 :12).

Kucita ulesi pa za cipulumutso ndi zauzimu miyoyo yathu imapita kucionongeko. Umatiletsa ife kupemphera, kutiletsa kufunafuna zinthu zakuya za Mulungu, umatiletsa kutenga malonjezano a Mulungu, umatitsogolera kucionongeko. Pamene Yehova walankhula nanu, kukufunsani kutl mupereke woyo wanu kwa lye lero, Satana akuuzani inu kuti mucite mawa, kapena tsiku lina, limene, pepani, simungathe kufikako; ndipo mumwalira wopanda cipulumutso ndi wopanda Yesu. Mulungu akuti, "Lero ngati mudzamva mau ace musaumitse mitima yanu" (Ahebri 3:7,8). Ndi anthu angati amene alangidwa cifukwa cakuzengereza cipulumutso pa masiku ena amene sanafikako? Tsiku la mawa silako ai.

Cigoba ca fulu n'cimene sing'anga amacita naco mankhwala, cimasonyeza macimo akukhulupirira asing'anga ndi amatsenga m'malo mwakukhulupirira Mulungu. Maka-maka m'nthawi za matenda ndi za mabvuto, timauzidwa kuitana pa Mulungu wa moyo amene ali pafupi pa nthawi ya cithandizo, m'malo mwakukhulupirira mwai kapena tsoka (Masalmo 37:23). "Yehova akhazikitsa mayendedwe a munthu". "Ndipo ngati adacita macimo, adzakhululukidwa kwa iye" (Yakobo 5:14-16). "Pakuti kukuzaku sikucokera ku m'mawa, kapena kumadzulo, kapena kucipululu. Pakuti Mulungu ndiye woweruza"

Copyright: ANGP

(Masalmo 75:6,7).Yehova analamulira ana a Israeli, nati, "Asapezeke mwa inu murithu wakupitiriza mwana wace wamwamuna kapena mwana wace wa mkazi ku moto wa ula, wosamalira mitambo, kapena wosamalira kulira kwa mbalame, kapena wanyanga. Kapena wotsirika, kapena wobwebweta, kapena wopenduza, kapena wofunsira akufa. Popeza ali yense wakucita izi Yehova anyansidwa naye" (Deuteronomo 18:10-12). "Kunja kuli agaru ndi anyanga, ndi acigololo, ndi ambanda, ndi opembedza mafano, ndi yense wakukonda bodza ndi kulicita" (Cibvumbulutso 22:15). Simudzabwera ku mizimu; kaya kwa iwo oneneratu za mtsongolo, kapena kufunsa za iwo, kucimwa pamodzi ndi iwo ndi kulangidwa ndi iwo. "Ine ndine Yehova Mulungu wanu" (Levitiko 19:31). "Ndipo pamene iwo adzati kwa iwe, Funsa alauli, ndi obwebweta, amene alira pyepye, nang'ung'udza; kodi anthu sadzafuna kwa Mulungu wao? Cifukwa ca amoyo kodi adzafuna kwa akufa? Kucilamulo ndi kuumboni. Ngati iwo sanena malinga ndi mau awa, ndithu sadzaona mbanda kuca" (Yesaya 8:19-20).

Pamene uwerenga kabuku kameneka, Mulungu alinkulankhula nawe, kuti utembenuke ndi kusiya zoipa zako ndi kugonjera moyo wako kwa Iye, koma mzimu wa fulu, umene uli mwa iwe, umalankhula kwa iwe kuti uzengeleze cisankho ca kwa Mulungu, ndi kuyesa kudzadza mtima wako ndi mantha. Abale anga, abwenzi anga, ndi dziko lapansi, adzati ciani ngati ndikhala Mkristu wepi-weni? Cidzacitika nciani ngati sindicita nao, camba, ndi zokondweretsa za m'dziko? M'malo mwakuona ulemerero wa Yesu Kristu, mtendere wace wodabwitsa, cimwemwe cace cosaneneka, moyo wodzara ndi cimwemwe, uyamba kuona zinthu zimene uyenera kutaya kapena kusiya. Pamene ulola Yesu Kristu kuti alowe mumtima mwako, kuopa munthu ngakhalenso kuopa imfa kumakusunga iwe kukangamira Satana. Koma Yesu Kristu anadza kudzapulumutsa iwo onse amene kupyolera mwa kuopa imfa, anali akapolo nthawi yonse ya moyo wao (Ahebri 2:14, 15). Kuzengereza kwa mzimu kuli kulimbikitsa mtima wanu mpaka ukhala ngati cigoba ca fulu.

5. KAMBUKU. (Leopard) Ndi nyama yoopsya ndi yankharwe. Ali yense amene amalamulidwa ndi mkwiyo amatsogozedwa ku macltldwe a mtima wakususuka. Ngati muyesa kulamulira mtima wanu woopsya posacedwa mkwiyo udzaturukanso. Kuli kwabwino kubvomereza kuti mkwiyo uli mu mtima mwanu ndipo mufunse Yesu kutl akuomboleni inu. "Musadzikwiyira inu nokha" (Genesis 45:5). "Leka kupsya mtima, nutaye mkwiyo; usabvutike mtima ungacite coipa" (Masalmo 37:8). "Kupweteka mtima nkwa nkhanza, nkwiyo usefuka; koma ndani angalakike ndi nsanje?" (Miyambo 27:4). "Usakangaze mumtima mwako ku kwiya; pakuti mkwiyo ugona m'cifuwa ca zitsiru" (Mlaliki 7:9). Koma tsopano tayani inunso r'nkwiyo (Akolose 3:8).

Anthu amantha ambiri amamwa kuti adzilimbikitse iwo eni ace pakucita maganizo oipa ndi nchito yoipa, koma "vinyo wao ndiwo ululu wa zinjoka ndi ululu waukali wa mphiri" (Deutoronomo 32:33). Ku bwezera kuli kwabwino kwa mtima woipa koma Mulungu ali m'bwezeri wathu. Yesu anati, "Kondani abale anu monga mudzikonda inu nokha" ndi "kukonda adani anu". Mulungu analonjeza kutikhulul ukira rriacimo athu ngati tikhulul ukir'a iwo oticimwira ife. Mzimu wonyinyirika uli woipanso pamaso pa Mulungu. Cilakolako ca nkhondo ndi kukhetsa mwazi ziri mumtima mwa munthu, ndipo ncifukwa cace mtendere weniweni uyenera kukhazikitsidwanso mu mtima.

6. NJOKA. (Snake) Idanyenga Hava m'munda wa Edeni ndi kuonoriga cigwirizano ca munthu ndi Mulungu. Satana, mngelo wakugwayo, anacita nsanje ndi Adamu ndi Hava pamene anaona iwo kuti anali oweruza dziko lonse, ogwirizana bwino ndi Mulungu, natenga malo a Lusifala. Cifukwa ca nsanje Satana anakonza njira ya cionongeko, ndipo anapambana mkuononga ciyanjano cao cabwino ndi Mulungu. Wansanje yemweyo amalowa mumtima wa munthu ndi kuononga cimwemwe m'mitima ya ena pamene aonakuti enawo ali okondwera ndi kukhala bwino. "Njiru imangouma ngati manda" (Nyimbo ya Solomo 8:6). Njiru imabweretsa maganizo oipa mumtima kuononga cimwemwe ca ena,



Copyright: ANGP

ndipo nthawi zina njiru irnatsoqolera kupha. Izi ndi zoona maka-maka kwa anthu ena okwatira. M'nchito ngakhalenso ndi zina zonse zolingana ndi moyo njiru imabweretsa usauki ndi udani. Ngakhale Akristu, alaliki ndi abusa siali omasuka ku njiru ngati Yehova atapatsa ena nchitoyi kopambana iwo. Acita bwino ngati atsogozedwa, ndi kudzazidwa ndi "cikondi ca Mulungu cimene cinapatidwa ponse ponse m'mitima yathu ndi Mzimu Woyera", kuti atumiki sadzaonongedwa ndi mzimu wa njiru.

7. CULE. (Frog) Asonyeza za macimo a umbombo ndi cikondi ca pa ndarama cimene ciri muzu wa zoipa zonse (1 Timoteo 6:10). Acule ena ku Kongo aonedwa alinkudya nyerere zambiri-mbiri mpaka. ataphulika nafa. Munthu waumbombo sapereka cithandizo kwa osauka, koma ayesa njira iyi ndi iyi, mokhulupirika kapena mosakhulupirika, kuunjika ndi kupindura cuma ca dziko lino lapansi, cimene pambuyo pace, dzimbiri ndi njenjete zidzaononga. Yesu mwini wace anati, "Musadzikundikire nokha cuma pa dziko lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri ziononga; ndi pamene mbala ziboola ndi kuba: koma mudzikundikire nokha m'Mwamba m'mene njenjete kapena dzlmblrl siziononga, ndipo mbala siziboola ndi kuba; pakutl kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso" (Mateyu 6:19,20). Akani ndi banja lace analangidwa cifukwa anakonda golidi ndi siliva ndi miyala ya ndarama ndi zobvala (Yoswa 7). Yudasi Isikarioti, wophunzira wa Yesu, anadzipacika yekha cifukwa ca cikondi ca pa ndarama cinampangitsa iye kupereka, Ambuye Yesu, Mphunzitsi wace. Si ndarama zimene ziri zoipa ai, kapena golidi, koma cikondi ca pa ndarama cimene cibisika mu mtima wa munthu.

Zikwi za amuna ndi akazi a mitundu yonse akuononga miyoyo yao ndi miyoyo ya mabanja ao cifukwa cakufuna kupeza kulemera kwa msanga mwa kucita juga, kucita maere ndi ndarama zambiri mwakupikisana pa njinga ndi kuthamanga ndi zina zotere. Cikhumbokhumbo cakufuna kulemera msanga popanda mabvuto cimatsogolera kukuba ndi kupha ndi kudzipha. Cikondi ca pa ndarama ndi umbombo cakhala kwa anthu ambirj monga cikondi cakuchuka; ndalama ingathe kukhala mphamvu ya ndale kulamulira ena, mphamvu ya pa cuma kufuna kutsendereza osauka, mphamvu ya pa mpingo, afuna dzina la mpingo kupambana la cifuniro ca Mulungu, kuletsa ena amene ayesa kutsata Yesu Kristu kopanda kutsata mpingo wace (Marko 9:38). Yesu anati, "Yang'anirani, mudzisungire kupewa msiriro uli wonse; cifukwa ·moyo wace wa munthu sulingana ndi kucuruka kwa zinthu zace ali nazo" (Luka 12:15). Mbiri ya munthu wopusa wa cuma iii conci: "Munda wace wa rnunthu mwini cuma umapatsa bwino. Ndipo anaganiza-ganiza mwa yekha nanena, ndidzatani ine, popeza ndiribe mosungiramo zipatso zanga? Ndipo anati, Ndidzatere: Ndidzapasula nkhokwe zanga, ndi kumanganso zazikuru, ndipo ndidzasungiramo zinthu zanga zonse, ndi cuma canga. Ndipo ndidzati kwa moyo wanga, moyo iwe, uli naco cuma cambiri cosungika kufikira zaka zambiri; tapumulatu, nudye, numwe, nukondwere. · Koma Mulungu anati kwa iye, Wopusa iwe, usiku womwe uno udzafunsidwa moyo wako; ndipo zinthu zimene unazikonza zidzakhala za ani? Atero iye wakudziunjikira cuma mwini yekha wosakhala naco cuma ca kwa Mulungu" (Luka 12:16-21 ). "Pakuti munthu apindulanji akadzilemezera dziko lonse, natayapo moyo wace? (Marko 8:36). "Musade nkhawa ndi moyo wanu, cimene mudzadya; kapena ndi thupi lanu, cimene mudzabvala ..... Komatu tafuna-funa Ufumu wace, ndipo izi adzakuonjezerani ..... Pakuti kumene kuli cuma canu, komweko kudzakhalanso mtima wanu" (Luka 12:22-34).

8. SATANA. (Satan) Ndi atate wa abodza onse ndipo m'modzi wa iwo arnene acita bodza, ali woyambitsa macimo osiyana, ndiponso ali wolamulira wa mtima. Yesu anati, "Inu muli ocokera mwa atate wanu mdierekezi, ndipo zolaka-laka zace za atate wanu mufuna kucita. Iyeyu anali wambanda kuyambira paciyambi, ndipo sanaima m'coonadi, pakuti mwa iye mulibe coonadi. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wace; pakuti ali wabodza, ndi atate wace wa ·bodza" (Yohane 8:44). Bodza laling'ono liri loipa cimodzi-modzi ndi lalikuru. Pali mabodza ena amene amayankhulidwa, kulembedwa, ndikucitidwa. Cinkhanira ncabodza pakuti zoonadi amadziyesera iye kukhala cimene iye sakadayenera



Copyright: ANGP

kukhala. Mulungu sanama ai ngakhale Mkristu sanganame ai (Tito 1 :2). "Tikati kuti tiyanjana ndi lye, ndipo tiyenda mumdima, tinama, ndipo siticita coonadi" (1 Yohane 1 :6). "Kunja kuli agaru ndi anyanga, ndi acigololo, ndi ambanda, ndi opembedza mafano, ndl yense wakukonda bodza ndi kucita" (Cibvumbulutso 20:15). Mulungu amadana ndi mboni yonama ndi wa bodza (Miyambo 6:19).

9. NYENYEZI (Star) lnena za cikumbumtima ca mu mtima wa munthu ali yense. Cikumbumtima pano ndi coipa kapena cafa kupyolera mwakulakwa kawiri kawiri mwakudziwa; nakhala akhungu ndi kusinthidwa kuti sicingathe kuweruza zocita zace zomwe. Cikumbumtima coipaci nthawi zina cimakhala cete, nthwai zina kubvutitsa kwambiri. Cimazengetsa pamene cikadayenera kupepesa, ndipo cimakupepesa pamene cikadayenera kuzengetsa, kapena cinataya nzeru zonse cifukwa cakutaya cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunziro a ziwanda ( 1 Timoteo 4:1,2; Ahebri 10:22).

10. DISO (Eye) Diso sa Mulungu liri ponse-ponse kuona ciri conse cocitika mu mtima. Palibe cobisika kucokera m'maso ace a moto, cifukwa cace amadziwa ndi kuona zonse zobisika m'maganizo ndi zitsimikizo za mtima. Ngakhale mutacita zoipa mumdima woti bii, m'nkhalango, m'dzenje ngakhale kwina kuli konse, Mulungu amaziona. (Diso m'cithunzi ici ligwirizana ndi nkhopeya munthuyo.)

11. MALILIME ANG'ONO AMOTO (Little tongues of fire) Malilime ang'ono amoto amene azungulira mtima afanizira za cikondi ca Mulungu pozungulira mtima wa wocimwa. Ngakhale Mulungu adana ndi ucirno amakonda munthu ndipo safuna imfa ya wocimwa, koma kuti alape ndi kukhala ndi moyo. Yesu anadza kudzapulumutsa ocimwa. Kumakhala cimwemwe cacikulu Kumwamba cifukwa ca wocimwa m'modzi wotembenuka mtima. Malilime ang'ono amoto amanenanso wotembenuka mtima. Malilime ang'ono amoto amanenanso za mwazi wa Yesu Kristu. "Nkhosa ya Mulungu imene icotsa macimo a dziko la pansi."

12. MNGELO (Angel) Mngelo afanizira Mau a Mulungu afuna kulankhula kwa wonyengedwa amuna ndi akazi ocimwa ndi kuwauza kuti iwo alape, ndipo alole kuunika ndi cikondi ca Mulungu mumtima mwao.

13. NKHUNDA (Dove) Nkhunda ifanizira Mzimu Woyera, mzimu wa coonadi umene umatsutsa cimo ndi cilungamo ndi ciweruziro. Pano tiona kuti Mzimu Woyera uli kunja kwa mtima wa Sukhala kumene ucimo ulamulira. Ngati cithunzi ca mtimaci cigwirizana ndi makhalidwe a mtima wanu, lirani kwa Mulungu, tsegulani mtima wanu kwa lye ndipo mulole kuwala kwa Mau ace kuwale mwa inu. "Ukhulupirire Ambuye Yesu Kristu ndipo udzapulumutsidwa". Mulungu ali cire, inde, walonjeza lye kusintha moyo wanu, ndi kukupatsani moyo watsopano, ndi mzimu watsopanonso mom'mo. Ici caonetsedwa mu cithunzi caciwiri.

Cithunzici cionetsa mtima wakulapa umene uyamba kufuna Mulungu. Mngelo ali ndi lupanga m'dzanja lace, Mau a Mulungu, amene ali "ofulumira ndi amphamvu ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konse-konse napyoza kufikira kugawira moyo ndi mzimu, ndi zimfundo ndi mafuta a m'mafupa, nazindikiritsa zolingirira ndi zitsimikizo za mtima" (Ahebri 4:12). Mau a Mulungu amukumbutsa iye kuti, "Mphotho ya cimo ndi imfa," ndikuti, "Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa,



Copyright: ANGP


ciweruziro" (Ahebri 9:27). Osakhulupirira ndi ocimwa adzalandira mphotho yao m'nyanja yotentha ndi moto ndi sulfure.

Pa dzanja lina mngelo wagwira cigapa. lei cikumbutsa ocimwa kuti tonse tiyenera kufa. Thupi lathu limene tilikonda kwambiri, kulibveka, kulidyetsa ndi kulikongoletsa, kulisunga bwino kulikwaniritsa zofuna zace. zoipa, lidzafa ndi kuola, ndipo mphutsi zidzadya, pamene moyo ndi mzimu wathu udzakhala ndi moyo nthawi zonse, ndipo tsiku lina lace udzaonekera kucimpando ca Mulungu ca ciweruziro.

## 2 CITHUNZI CACIWIRI

Pano tiona kuti wocimwa alikuyamba kumvera uthenga wa Mulungu ndi kutsegula mtima wace ku cikondi ca Mulungu. Mzimu Woyera uyamba kuwala mu mtima wa wocimwa. Kuyera kwa Mulungu kulowa m'kacisi wace ndikucotsa mdima. Pamene kuwala kwa Mulungu kulowa, mdima umacoka. Cimo, limene limafanizidwa ndi zinyama za mtundu rntundu, ziyenera kuthawa. Ngfukwa cace, wowerengawe, Iola Yesu, Kuunika kwa dziko lonse lapansi, kulowe mu mtima mwako, ndi mdima ndi nchito ya mdima zicoke mu mtima, monga kwaonetsedwa mcithunzici. Yesu anati, "Ine ndine kuwala kwa dziko lapansi, ngati wina atsata Ine, sadzayenda mu mdima" (Yohane 8:12). Sudzapambana kucotsa mdima mu mtima mwako ndi mphamvu ya ·;we wekha, nzeru yako, kapena ndi nzeru ya anthu. Njira yapafupi-fupi, yotsimikizika ndi yocita msanga, ndiyo kulola Yesu, kuunika, adze, ndipo mdima, umene uli ucimo udzacoka. Mwezi ndi nyenyezi ningathe kutipatsa ife cithandizo cakuwala mu mdima, koma pamene dzuwa latuluka, ndipo mdima pamodzi ndi kuwala kwapang'ono kumacoka. Yesu ndi dzuwa lacilungamo. Pamene analowa mkacisi ku Yerusalemu, anawapitikitsa onse amene anagulitsiramo ng'ombe zamphongo, nkhosa ndi nkhunda, ndi kutaya pansi ndarama zosinthanitsa, ndikuti, "Pakuti kwalembedwa, Nyumba yanga idzachedwa nyumba yamapemphero; koma inu mwaisandutsa nyumba ya malonda" (Mateyu 21 :31 ).

Copyright: ANGP




Mtima wanu uli nyumba ya Mulungu, kacisi wa Mulungu. Iye afuna kuti akhalemo, kuukongoletsa iwo, kuudzaza ndi kuunika, cikondi ndi cimwemwe. Yesu sanabwere kokha kudzakhululukira ife macimo athu, koma anadza kudzatipulumutsa ife ndi kutikhazika ife mu afulu kucokera kumptiamvu ya Satana ndi ucimo. "Ngati Mwana (Yesu) adzakuyesani inu aunnu, mudzakhala mfulu ndithu" (Yohane 8:36).

Copyright ANGP

3 CITHUNZI CACITATU

Cithunzi ici citionetsa kakhalidwe kace ka mtima umene walapa ndithu kuucimo. Iye tsopano aona kukula kwace ndi kuipitsitsa kwace kwa macimo ace amene Yesu anafera pa mtanda. Ayamba kuona mtanda umene mngelo, Mau a Mulungu, aulula kwa iye, ndikuphwanya tsopano mtima wace wacisoni, ndipo azindikira ndikumva cisoni pa zolakwa zace anazicita. Aonanso cikondi cacikuru ca Mulungu r:nwa Kristu Yesu, cikondi cimene cisungunula mtima wace, makamaka pamene ayamba kuzindikira kuti Yesu Kristu, rnwana wa Mulungu, anadza kudzatenga macimo ace onse pakufera Iye m'malo mwace pa mtengo wa tembelelo.




Kuzunzidwa kwa Yesu, kubvekedwa cibakuwa caminga ku mutu kwace, ndi kukhomedwa misomali m'manja nd1 m'mapazi ace, kufa kwace . pamtanda cifukwa ca macimo athu, zimcititsa munthu wolapayo atembenuke mtima. Pamene awerenga Mau a Mulungu m'mene angathe kuona yekha ngati mkalilole, azindikira pang'ono ndi pang'ono m'mene wataikila kunja kutali ndi Mulungu ndi m'mene wacimwira malamulo a Mulungu. Cisomo cacikuru cimamgwira iye, ndipo pamene mtima wace uulula zonse pa maso pa Mulungu ndimisozi ndi kulira kwakukuru, Yesu adza pafupi ndi lye. Cikondi ndi mtendere wa Mulungu zilowa mu mtima mwace pamene ayamba kuzindikira kuti, "Mwazi wa Yesu Kristu, Mwana wa Mulungu, utisambitsa ndi kuticotsera ife macimo athu onse" (1 Yohane 1 :7). "Yehova ali pafupi ndi iwo a mtima wosweka, apulumutsa iwo a mzimu wolapadi" (Masalmo 34:18). Ndiponso mau a Mulungu anena, "Koma ndidzayang'anira munthu'yu amene ali waumphawi, ndi wa mzimu wosweka, nanthunthumira ndi mau anga" (Yesaya 66:2). Mzimu Woyera unong'oneza mau a Yesu kwa iye, "Mwana, khala wa makhalidwe abwino, macimo ako akhululukidwa."

Adakayang'anabe pa mtanda ndi mwazi wa Yesu unakhetsedwa pa mtanda, ndi kukhulupirira kuti zonsezi zinacitidwa cifukwa ca lye ayamba kuzindikira kuti katundu wa ucimo wacotsedwa, pakuti Yesu anyamula zowawa zathu ndi kutenga nsoni zathu; kuti "Koma lye analasidwa cifukwa ca zolakwa zathu, natundudzidwa cifukwa ca mphulupulu zathu; cilango cotitengera ife mtendere cinamgwera lye" Kuti "Ndipo. Yehova anaika pa lye mphulupulu ya ife tonse" (Yesaya 53:5).

Mzimu Woyera ndi cikondi ca Mulungu zitenga malo onse mu mtima wotsukidwa, pamene aona ndi cikhulupiriro pa mtanda paja mwazi wa Yesu, umene unakhetsedwa kuticotsera macimo athu, lye ayamba kuzindikira kuti macimo ace akhululukidwa, ndi kulandira mu mtima mwace kuti mwazi wa Yesu, Mwana wa Mulungu, wayeretsa macimo ace onse (1 Yohane 1 :7). lye adziwa tsopano kuti, "lye amene akhulupirira mwa Yesu sadzalangidwa, koma adzakhala ndi moyo osatha" (werengani 1 Akorinto 6:10, 11 ). Pakuti mwa Yesu, "tiri ndi maomboledwe mwa mwazi wace, cikhululukiro ca macimo, monga mwa kulemera kwa cisomo cace" (Aefeso 1 :7). Zilakolako zoipa za thupi zapereka malo ku zofuna zakuya za Yehova, ndipo munthuyo ayamba kumpembedza Mulungu "amene anayamba kutikonda ife". M'malo mwakukonda dziko lapansi ndi zinthu za dziko lapansi, akonda Mulungu ndi zinthu za Mulungu.

Copyright ... ANGP

M'cithunzi ici ncifukwa cace, tipeza nyama zimene zifanizira macimo, ziri kunja kwace kwa mtima wace, ngakhale Satana safuna kusiya malo ace akale.

MTIMA WOLAPA. (The Repenting Heart.) Aceuka m'mbuyo ndi kukhala ndi ciyembekezo cakupeza mpata kaciwirinso. Ncifukwa cace Yesu anaticenjeza ife tipenyetsetse ndi kupemphera, kukaniza Satana kuti athawe kwa ife.

## 4 CITHUNZI CINAI




Cithunzi ici cionetsa Mkristu amene wapeza mtendere ndi ciombolo mwa kudzipereka nsembe kwa Ambuye Yesu Kristu mpulumutsi wathu, ndi cifukwa cace kudzitama sikuli kanthu "koma mu mtanda wa Ambuye wathu Yesu Kristu, amene mwa lye dziko lapansi lapacikidwira ine, ndi ine ndapacikidwira dziko lapansi" (Agalatiya 6:14): Yesu anafa pa mtanda kuti ·ifenso, tikakhale titafa ku macimo, tikakhale ndi moyo kutsata cilungamo" (1 Petro 2:24); Mkristu anafa ku za dziko. Talamulidwa kuti "tiyendeyende mwa mzimu kuti tisafitse zilako-lako za thupi" (Agalatiya 5:16,25).

Ciumuni cimene Ambuye Yesu anamangidwa pambuyo pace pamene anacotsa cobvala cace, caonetsedwa m'cithunzi ici ca mtima, pamodzi ndi zikoti ndi zikwapulo zimene ankharwe anam'menya nazo. Anamenyedwa cifukwa ca macimo athu cifukwa "cilango. cotitengera ife mtendere cinangwera iye". Mfumu Herode ndi anthu ace anamnyoza, ndi pambuyo pa kum'kwapula iye naluka korona wa minga, nambveka pa mutu pace m'malo mwa korona wa golidi, ndikumpatsa ndodo yabango m'dzanja lace mmalo mwa ndodo ya cifumu, ndipo anam'gwadira lye namnyoza lye, anena, "Tikuoneni, Mfumu ya Ayuda!" Ndipo anampanda lye pamutu pace ndi bangolo, nam'thira malobvu. Pamene anatha kumnyoza kwambiri anapita naye kukampacika.

Pali Akristu ambiri amene amapemphera m'machalichi, amene amadya mgonero wa Ambuye, nayimba nyimbo za Mulungu, komabe ndi nchito zao zoipa amampacikanso Ambuye". "Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba, koma wakucita cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba" (Mateyu 7:21-27).

Pa cithunzipa muonanso thumba la ndarama la Yudasi, amene anapereka Ambuye Yesu ndi kum'gulitsa lye ni ndarama makumi atatu a siliva, cifukwa ca cikondi ca ndarama cimene cidagwira

mtima mwace ndi kucititsa khungu maganizo ace. Muonanso nyali ndi unyolo, anagwiritsira nchito asilikali ameneanagwira Yesu usiku uja. Maere, a amene nthawi zambiri amacitika mwampikisano, analikugwiritsidwa kuti adziwe cobvala ca Yesu cidzakhala ca yani; kotero ndiko kukwaniritsa Mau a Mulungu onena kuti, "Anagawana zobvala zanga, nacita maere pa malaya anga" (Masalmo 22:18). Anatenga ciri conse cimene Yesu anali naco, Koma Mwini wace anamukana, nanena, "Sitifuna kuti iye atilamulireife".

Munthu amafunitsitsa kulandira madalitso onse kucokera kwa Mulungu, mvula yonse ndi kuwala konse kwa dzuwa, koma safuna kumvera cilamulo ca Mulungu. Kwa ambiri, Mulungu ali wabwino kuwathandiza m'nthawi za mabvuto ndi zowawa.

Msilikazi anam'baya Yesu mkondo m'nthiti ndi mumtima wace, munaturuka mwazi ndi madzi pomwepo" (Yohane 19:33-37). Tambala asanalire Petro anamkana katatu Yesu, koma pambuyo analapa ndi misozi yowawa. Nanga iwe, ulinkubvomera Yesu m'mau ndi m'nchito kodi? Kapena uli ndi manyazi kucita zimenezi pa maso pa anthu? Yesu anati, ''Yense amene adzandikana Ine pamaso pa anthu, Inenso ndidzamkana iye pamaso pa Atate wanga wa Kumwamba" (Mateyu 10:32,33).

Yesu anatinso, "Ndipo iye amene satenga mtanda wace, natsata pambuyo panga, sayenera Ine" (Mateyu 10:38). Odala iwo amene aima pa thanthwe, ndiye Yesu Kristu.

Thanthwe long'ambikatu,

Ndibisale momwemu!

Madzi ndipo mwaziwo Zoturuka m'nthitimo,

Zinditsuke m'mtima mbu!

Zindilimbikitsetu.

## 5 CITHUNZI - THUNZI CACISANU

Cithunzi ici cionetsa moyo wotsukidwa ndi woyeretsedwa wa wocimwa amene wapulumutsidwa ndi cisomo ndi cifundo ca Mulungu. Tsopano ali kacisi wa Mulungu weni-weni, nyumba ya Mulungu yokhalamo Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera, molingana ndi lonjezamo la Ambuye wathu Yesu Kristu, "ngati wina akonda Ine, adzasunga mau anga: ndipo Atate wanga adzamkonda iye, ndipo tidzadza kwa iye, ndipo tidzayesa kwa Iye, mokhalamo" (Yohane 14:23). Mulungu apereka ulemu, adalitsa nakweza munthu mwa Yesu Kristu (Luka 1:52).

Tsopano Mtima wakhala kacisi wa Mulungu weni-weni. Ucimo wacotsedwamo. M'malo mwa zirombo zoikidwa ndi Satana, atate wabodza, timaona Mzimu Woyera, Mzimu wa Coonadi, wakhala mu mtima . Kucokera kukhala mpando woipa wa macimo, mtima tsopano wakhala ngati mtengo wokongola wobala zipatso,

kapena munda wopatsa zipatso za uzimu, monga ngati, cikondi, cimwemwe, mtendere, kueza mtima, ciletso, cifundo, kukoma mtima cikhulupiriro cifatso ndi zipatso zina zimene zimkondweretsa Mulungu ndi munthu. Ali thambi yobala cipatso ya Mpesa weni-weni, ndiye. Ambuye wathu Yesu Kristu.

Njira yobisika yobalira zipatso ndiyo kukhala mwa Yesu Kristu ndi Yesu mwa iye mwa mau ace (Yohane 15:1-10). Monga wadzadzidwa ndi kubatizidwa ndi Mzimu Woyera, ali nayo mphamvu yakugonjetsa thupi ndi zofuna zace, ndi kupacika umuntbu wakale. Mwa mphamvu ya Mzimu Woyera

Copyright: ANGP

akhoza kuyenda mwa Mzimu ndi kugonjetsa za thupi. Sakhalanso mwa zimene aziona, kapena azimva ndi zimene aziganizira, koma mwa cikhulupiriro cifukwa cikhulupiriro ca mwa Yesu Kristu ndico cigonjetso cogonjetsera za m'dziko. Ndipo akhala moyo ndi ciyembekezo ca coonadi nalimbikitsidwa ndi ciyembekezo ca kubweranso kwa Yesu Kristu. Akhala ndi moyo mwa cikondi ca Mulungu cimene cikhala ku nthawi zonse.





"Odsia ali oyera mtima, cifukwa adzaona Mulungu" (Mateyu 5:8). Mfumu Davide, angakhale anali wolemera ndi kupambana kwace pa adani ace, anadziwa kuti nkhondo yaikuru iii mumtima mwace momwe, ndipo pozindikira zosowa za mkati mwa mtima wace, anapemphera, 11Mundilengere mtima woy-. era, Mulungu, mukonze mzimu wokhazikika m'kati mwanga" (Masalmo 51 :10). Palibe munthu angadziyeretse yekha mtima wace kapena kudzilengera mtima wabwino, koma kuti adze kwa Mulungu ndi kulapa monga adacita Davide pofunsa Mulungu kuti amlengere iye mtima watsopano m'kati mwace. Mulungu afuna kucita kanthu katsopano m'moyo mwako. Kubadika zigamba nsaru zong'ambika za cilungamo canu ndl malonjezano anu onama sikudzapangitsa mtima wanu kukhala malo abwino a Mulungu. lye ali ofuna kukuthandizani inu, pakuti ndiye amene analonjeza nanena, 11Ndipo ndidzakuwazani madzi oyera, ndipo mudzakhala oyera; ndidzakuyeretsani kukucotserani zodetsa zanu zonse, ndi mafano anu onse. Ndipo ndidzakupatsani mtima watsopano, ndi kulonga m'kati mwanu mtima watsopano; ndipo ndidzacotsa mtima wamwala m'thupi, lanu ndi kukupatsani mtima wam'nofu. Ndipo ndidzaika mzimu wanga m'kati mwanu, ndi kukuyendetsani m'malemba anga; ndipo mudzasunga maweruzo anga ndi kuwaclta" (Ezekieli 36:25-27). lei ndi citanthauzo cace ca cipangano catsopano cimene Mulungu anasindikiza ndi mwazi wa Mwana wace Yesu Kristu, Ambuye wathu.

Pa cithunzi ici tionanso mngelo alikuonekera kaciwiri. Angelo amatumikira iwo amene adzalandira moyo wosatha, ndipo amazongurira ndi kucinjirira iwo akuopa Yehova (Masalmo 34:7; 91 :11; Daniel 6:22; · Mateyu 2:13; 13:19; 18:1 O; Macitidwe 5:19; 12:7-10).

Ndiponso Satana akuonekera m'cithunzithunzi ici.Waima moyandikira ku mtima monga afuna kubwerera mu mtima m'mene analimo kale. Cotero tauzidwa kuyang'ana ndi kupemphera pakuti "mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobunma, ayendayenda ·ndi kufunafuna wina akamulikwire" (1 Petro 5:8); .Nthawi zambiri Satana adzionetsa ngati mngelo wa kuunika, kuti anyenge Akristu

osadikirira ndi zilakolako za dziko lapansi ndi macenjero ace. Koma tikarnkana Satana, adzatithawa ife (Yakobo 4:7).

## 6 CITHUNZI-THUNZI CACISANU NDI CIMODZI



Cithunzi-thunzi ici ndi ca munthu wobwerera mbuyo. Diso lace limodzi layamba kutsinzina kuonetsa kuti tsopano moyo wa Cikristu cace ulikuzizira ndi kugona, ndipo diso lina lirikuyang'ana-yang'ana popanda manyazi kuti lipange cikondi ndi dziko. Kuwala kwace kwa mkati kwada, ndipo zizindikirozo za mumtima mwace, zimene zinaonetsa kukonzeka kwace kwa kubvutika ndi Kristu, tsopano zafooka, ndipo· siziri zoongoka. Munthuyu ali wozunguliridwa ndi mayesero amene alikuwagonjera m'malo mwa kupirira. M'malo mwa kumvera Mau a Mulungu, wayamba tsopano kuvera mau a Satana ndi malingaliro ace ndi malonjezo ace abodza. Ngakhale mwina akhale munthu wopita ku charichi kuti maonekedwe a pemphero abise macitidwe ace a dziko amene alikucita, cikondi ca kwa Mulungu sicili mumtima mwace. Cacokeratu! Ali ndi maganizo awiri, ndipo cifukwa cace alikukayika! Alikuyamba kusirira zinthu za dziko lapansi poyerekeza kuti amkonda Mulungu ! Nyenyezi ya mu mtima mwace, ndiyo cikumbumtima, yazima! Mtanda sulikusenzedwa ndi cikondwerero, koma ukhala ngati cinthu cosafunika cimene ciri colemera. Cikhulupiriro cace ciri kukayika-kayika, ndipo iye waleka kupembedza Mulungu.

Wayamba kukhala wosasamala ndipo m'makhalidwe ayamba kupatsa malo Satana amene alikubisalira mtima wace. Akondwera ndi zinthu za dziko lapansi koposa kukondwera ndi okhulupirira oona. Mzimu wa ntiwatiwa, ndiwo kunyada, ulikuyesa kulowanso! Munthuyu waiwala kuti anapulumutsidwa ndi cisomo cokha. Kuledzera kugogoda pa lchomo ndikufuna cipata coloweramo. Kapena kulikumuyesa iye kuti alawe pang'ono cakumwa, ndi kumuuza kuti mowa wowawa pang'ono uli bwino.Sadziwa kuti mowa wowawa pang'ono uli ngati mtsinje waung'ono umene umatsogolera kum'mtsinje waukulu woledzeretsal Kapenanso mkazi aphikira mwamuna wace ndi abwenzi ace mowa, koma iye mwini aukana ndi kunena, "lne, sindikumwa mowa". Komabe, iye atsogolera ena kuti anyengedwe ndi mzimu wakuledzera! Ciwerewere ndi cigololo zimayesa Mkristu ndi kuyesedwa kwa Gehena! Kapena ayamba kumvetsera ndi cimwemwe zokambidwa zonyansa, kukondwera ndi magulu oipa, kucita zoipa, kubvina camba coipa. Kapena wina amuuza kuti njira ya "Cikristu" m'mene amuna ndi akazi abvinira pamodzi ndiyo yabwino koma kuti nkulakwa kubvina mabvinidwe acikale.

Sazindikira kuti malo onse m'mene anthu abvinira ndimo mocititsa cilakolako, ndipo kuti kubvinirana amuna ndi akazi ndiko koipa koposa kubvina kwa mtundu wina. Njira ya "Cikristu" ya kusuta fodya iii yoipa ngati njira ya kale ya kusuta fodya, pakuti m'njila zonse ziwirizi, anthu amasuta kwambiri usana ndi usiku !

Munthu amene alikubaya mtima wa munthuyu wa pa cithunzithunzipa afanizira iwo amene amanyoza Cikristu ndi kucineneza. Ndi zonena-nena za malilime ao ndi kunyoza kwa milomo yao abaya ndi kupweteka mitima ya Akristu. Munthu wa mtima wogawidwa sangathe kulaka nkhondo yotero. Ayamba kuopa munthu koposa Mulungu ndipo cifukwa cakuopa cimene munthu adzacinena ndi kucicita, akhala kapolo wa munthu ndipo acoka kwa Mulungu. Maganizo oipa ndi kupsa mtima msanga zidzionetsa mu nthawi yamabvuto ndi ya zokhumudwitsa ndipo zilowa mwa mphamvu, Njoka yansanje imene ioneka pamene ena apambana anzao ilowa mosadziwika, ndipo ngati ipatsidwa mwai waung'ono, idzatsegula citseko ca udani ndi kunyada.

Nkwapafupi kuti cikondi ca pa ndarama cikwawire m'mitima yathu tikapanda kumvera macenjezo a Ambuye wathu Yesu amene anati, "Dikirani ndipemphera kuti mungalowe m'kuyesedwa" (Mateyu 26:41 ). "Cifukwa cace iye wakuyesa kuti ali ciriri, ayanganire kuti angagwe" (1 Akorinto 10:12). Tibvale zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kuclrirnika pokana macenjerero a Satana (Aefeso 6: 11-18).

## 7 CITHUNZITHUNZI CACISANU NOi CIWIRI


Cithunzithunzi ici cionetsa cikhalidwe ca munthu wobwerera mbuyo amene kale anaunikiridwa nalawa mphatso ya Kum.. wamba, nakhala wolandirana nave Mzimu Woyera, komatu anagwanso. Cionetsanso khalidwe la munthu wosaternbenuka mtima; ngakhale "Uthenga Wabwino" unalalikidwa, nupatsidwa, nuululidwa kwa iye. Munthu amene aumitsa mtima wace pamene Yehova alankhula naye mopempha adzakhala woipaipade ngakhale angayese kudzilungamitsa.

Yesu ananena za munthu wakubwerera mbuyo ndi mau awa: "Pali ponse mzimu wonyansa ukatuluka mwa munthu, upyola malo opanda madzi nufuna-funa mpumulo; ndipo posaupeza unena, ndidzabwera ku nyumba kwanga kumene ndinatulukako; ndipo pofika; uipeza yosesa ndi yokonzeka. Pomwepo upita nutenga mizimu yina isanu ndi iwiri yoipa yoposa uwowo; ndipo ilowa nikhala momwemo; ndipo makhalidwe otsiriza a munthu uyu aipa koposa oyambawo" (Luka 11 :24-26).

"Kwacitika kwa iye monga mwambo unati: Galu wabwerera ku masanzi ace, ndi nkhumba idasambayi yabwerera kukunkhulira m'thope" (2 Petro 2:22).

Malembo amenewa afotokoza za khalidwe la wobwerera m'buyo ndi wosatembenuka mtima wace woipa. Ucimo ndi kunyenga kwace konse zabwereranso kudzakhala ndi kudzalamulira mtima. Ngakhalenso nkhope yace, nthawi zina, imaonetsa cikhalidwe ca mtima wace. Nkosatheka kuti mtima ukhale kacisi wa Mulungu ndipo nthawi yomweyo, nyumba yokhalamo Satana. Mngelo, ndiye Mau a Mulungu, adzacoka mwacisoni, alikuyang'anabe m'mbuyo ndi ciyembekezo cakuti iyeyo nthawi zina angathe kutembenuka monga mwana uja wolowerera, "Ndipo analaka-laka kukhutitsa mimba yace ndi makoko amene nkhumba zimadya, ndipo palibe munthu anam'ninkha kanthu. Ndidzanyamuka ndipite kwa atate wanga, ndipo ndidzanena naye, atate ndinacimwira Kumwamba ndi pamaso panu; Sindiyeneranso konse kuchulidwa mwana wanu" (Luka 15:18). Atate poona mwana wace anamukhululukira nakhalanso ndi iye. Koma pa nthawi iyi m'cithunzithunzici, palibe cizindikiro ceni-ceni cakutembenuka ndi kubwerera kwa Mulungu kuti alandire cikhululukiro pamapazi a Yesu. Cikumbumtima cace calocedwa monga ndi citsulo ca moto, ndipo sicilankhula. Ali nao makutu koma sakumva kuitana kwa Yesu Kristu. Ali nao maso koma sangathe kuona dzenje lacilango limene liri pafupi ndi mapazi ace. Sakumvanso manyazi popitiriza macimo ace. Satana wadza kudzalamulira mu

mtima mwace ndipo wakhala pa mpando wacifumu wakuweruza. Kuli kotheka kuti anqadzitukumulebe ndi maonekedwe ace abwino. Koma maonekedwe ace ali monga Mau a Mulungu amene ati, "Koma adzala m'katimo ndi mafupa a anthu akufa ndi zonyansa zonse" (Mateyu 23:27).



Atate wamabodza alirikukhala m'malo a Mzimu wa Coonadi. Cirombo ciri conse, cimo liri lonse limatsagana ndi mzimu woipa umene tsopano wasunga mtima wace. Ngakhale akadafuna kudzimasula kwa nsinga za mzimu woipa, alikumangidwa ndi iwo. "Munthu wopeputsa cilamulo za Mose angofa wopanda cifundo pa mboni ziwiri kapena zitatu: ndipo mutani, kulanga koposa kotani nanga adzayesedwa woyenera iye amene anapondereza Mwana wa Mulungu, nayesa mwazi wa cipangano unayeretsedwa nao cinthu wamba, nacitira cipongwe Mzimu wa cisomo" .. (Ahebri 10:28,29; 2 Petro 1 :14).

Ngati cithunzi ici cigwirizana ndi makhalidwe a mtima wanu, bwenzi langa, pfuulirani kwa Mulungu mosacedwa, kucokera pansi pa mtimawanu. "Akhoza kukupulumutsani inu", ndipo ali wokhoza ndi wokonzeka kukuhulululukirani macimo anu onse ngati mudza ndi mzimu wakulapa moonadi. Angathe kumanga Satana ndi mizimu yace yonse ya mdima, ndi kuwaturutsa kucokera mumtima mwako, ngati ulola ·kuti lye acite comweco. Idzani monga wakhateyo amene anadza kwa Yesu nanena, "Ngati mufuna, mukhoza kundikonza".

Yesu anayankha nati, "Ndifuna; Khala wokonzedwa" (Marko 1 :40,41 ). Koma ngati upitirira kuumitsa mtima wako ndi kukonda nchito za mdima koposa kuunika, palibe ciyembekezo, palibe cithandizo pakoti uli kusankha imfa m'malo mwa moyo "Pakuti mphotho ya·ucimo ndi imfa". (Aroma 6:23).

Copy... ANGP

8 CITHUNZI-THUNZI CACISANU NDI CITATU





Pano tiona munthu wozengereza kapena woumitsa mtima wace alikuyandikira imfa, thupi lace liri lodzala ndi zowawa ndi moyo wace wadzazidwa ndi mantha a imfa. Imfa, yabwera m·wadzidzidzi ndi pa nthawi yosafunika. Zokondweretsa zakunyenga zapita, ndipo coopsya mphotho ya ucimo tsopano cilikukomana naye. Masautso a Gehena alikumgwera iye. Ngakhale tsopano afuna kupemphera, apeza kuti sangathe kugwirizana ndi Mulungu amene cikondi cace anacikana kale lomwe. Abwenzi ace akale alinkucita mantha kukhala pafupi ndi iye ndipo mau ao acabe sangathe kumthandiza tsopano. Cuma cace sicingathe kuonjezera masiku amoyo wace, ngakhale kupulumutsa moyo wace, ngakhale ku thandiza ululu wa moyo wace. Apeza kuti ncosatheka kuganizira za Mulungu pakuti Satana samupatsa mwai wakutero.

Zinthu zonse anazikonda nazikhalira, tsopano zilikumjeda iye, ndipo ngakhale m'busa wace wosakhulupirika kapena wosatembenuka sangathe kumthandiza iye tsopano cifukwa anakana cisomo ca Mulungu nagwa pansi pa kutsutsa kwa cilamulo. Ayamba kuzindikira kuti,

"Kugwa m'manja a Mulungu wamoyo nkoopsa" (Ahebri 10:31 ). Anayembekeza kuti akadakwaniritsa mlandu wace ndi Mulungu tsiku lina, kapena pakufa pace, koma tsopano apeza kuti nthawi yampitirira. Zikwi za anthu zimafa mwadzidzidzi mopanda mwai wakufuna Mulungu pa nthawi yakufa yao. Cifukwa cace kuli kofunika kufuna Yehova popezeka Iye. M'malo mwakum- vetsera mau a bwino ndi opulumutsa a Mulungu, munthu wakufayu, wocimwa ndi wokana cisomo ndi cikondi ca Mulungu munthawi ya moyo wace, ayarnba tsopano kumva mau a ciweruziro cace kwa Mpulurnutsi amene iye anam kana, amene anena, "Cokani kwa Ine wotembereredza inu, ku moto wa nthawi zonse wokolezedwera mdierekezi ndi amithenga ace" (Mateyu 25:41 ). "Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzl, ndipo atafa, ciweruziro" (Ahebri 9:27).

Copy... ANGP

## 9 CITHUNZITHUNZI CA CISANU NDI CINAI




Cithunzithunzi ici cifanizira Mkristu amene alikupirira ndi kulaks mabvuto amoto ndi mayeso. Pamene iye alikuyesedwa munjira zonse, akhalabe wolimba nji cilimbikire mpaka cimaliziro, munthu wolakatu mwa Yesu Kristu. Sanangolowa njira ya Cikristu ai, koma alikupiriramo, ndi kuthamangamo mosayang'ana ku dzanja lamanja kapena lamanzere, koma, "Kwa Yesu, Woyambira ndi Womariza wa cikhulupiriro catbu" (Ahebri 12:1,2).

Satana ndi anthu ace azungulira mtima wokhulupirira kuti ayese kumsoceretsa mwanawa Mulungu. Kunyada, cikondi ca pa ndarama, cigololo ndi zina zotero ziri pano. M'malo mwa kambuku, tiona tsopano bulu, pakuti nthawi zambiri ucimo umayandikira ife munjira zosiyana-siyana kuti ubisale m'dzina lina. Koma Mkristu woyang'anitsitsa amaona ucimo pamene ubwere munjira ya cipembedzo kapena monga kuunika kwa mngelo, pakuti Mau a Mulungu ndi Mzimu wa Coonadi umamtsogolera iye ku coonadi conse. Munthu wokhala ndi cikho ca vinyo m'dzanja lina, abvina mozungulira Mkristu kuti amuyese iye ndi zokondweretsa za dziko lapansi. Mkristu woyeretsedwa sabvutika nazo cifukwa wapacikidwa ndi Kristu ku ucimo ndi zinthu za dziko lapansi. Munthu waciwiri m'cithunzithunzi alikubaya Mkristu ndi mkondo. Kulankhula koipa, maugogodi, kunyoza ndi kuopseza kupyolera mu adani a Mulungu (ndipo nthawi zambiri kupyolera mwa okhulupirira omwe) zilikubaya mtima wokhulupirira woona. Koma ali wakufa ku cimene anthu acinena, koma akumbukira mau a Yesu. "Odala muli inu angosamala cimene anena Mulungu yekha. M'mene adzanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa ziri zonse cifukwa ca lne. Sekerani, sangalalani.: cifukwa mphotho yanu ndi yaikuru m'mwamba". (Mateyu 5:11-12).

Ucimo, thupi, ndi Satana zili· kuyesabe ndi mphamvu zao zonse kusianitsa Mkristu kucokera ku cikondi ca Mulungu. Koma ndi cimwemwe cacikuru ndi cikhulupiriro angathe kunena .kuti, "Adzatisiyanitsa ndani ndi cikondi ca Kristu? Nsautso kodi, kapena kupsinjika mtima, kapena ku zunza, kapena njala, kapena usiwa, kapena zoopsya, kapena lupanga kodi? (Aroma 8:35). "Koma m'zonsezi, ife tili mdithu mwa iye amene anatikonda" (Aroma 8:37). Pakubvala zida zonse za Mulungu, angathe kukhala m'zoipa tsiku lonse ndi kupambana rnayesero onse mwa Yesu Kristu amene anapambana m'zonse kuti, kupyolera mwa lye, tingathe kupambana ndi kupeza korona wa ulemerero.

NYENYEZI ya cikhumbumtima yace iii yooneka ndi yowala. Mtima wace uli wodzazidwa ndi cikhulupiriro ndi Mzimu Woyera. Mngelo, wofanizira Mau a Mulungu, amkumbutsa iye za malanjezano

Copy... ANGP

a mtengo wapatali amene anapatsidwa kwa iye kuti akapambanire nao ndi kukhala olimbikira potsiriza. "Kwa iye amene alakika ndipo adzampatsa kudya za ku mtengo wa moyo umene uli m'Paradiso wa Mulungu". "lye amene alakika sadzacitidwa coipa ndi imfa yaciwiri" "Kwa iye wolakika, ndidzampatsa manaobisika, ndipo ndidzampatsa mwala woyera, ndi pa mwalawo dzina latsopano lolernbedwapo, mosalidziwa munthu ali yense koma iye wakuulan dira". "Ndipo iye amene alakika, ndi iye amene asunga nchito zanga kufikira citsiriziro, kwa iye ndidzampatsa ulamuliro wa pa amitundu". "lye amene alakika adzambveka motero zobvala zoyera". "lye wakulakika, ndidzamyesa iye mzati wa m'kacisi wa Mulungu wanga, ndipo kuturuka sadzatulukamonso". "lye wakulakika, ndidzampatsa akhale panbsi pa ine pa mpando wacifumo wanga monga inenso, ndinalakila, ndipo ndinakhala pansi pa Atate wanga pa mpando wacifumu wace" (Cibvumbulutso 2:7, 11; 17-26; 3:5, 12-21 ).

THUMBA LOTSEGUKA LA NDARAMA litisonyeza kuti si mtima wace wokha komanso ndarama zace zipatulidwa kwa Mulungu. M'malo mwa kuwaza zinthu za dzikolapansi, alikuthandiza aumphawi, alikupereka cakhumi (gawo Hmodzi la magawo khumi) ndi zopereka, kapena cuma cace conse, kwa Mulungu kuti agwiritse nchito ciri conse ku ulemerero wa Mulungu.

MKATE NDI NSOMBA zisonyeza kuti ali ndi moyo woyera ndi wabwino. Sadziipitsa yekha ndi zoledzeretsa kapena kudya mwazi, kapena cimene cangofa pa cokha, kapena cakudya cina coipa.Sangotaya ndarama zace, ngakhale kuononga thupi lace (Limene liri kacisi wa Mulungu) mwa kudya kapena kusuta fodya mwa njira iri yonse, ngakhalenso kugwiritsa nchito m'bulu wa mankhwala oipa korna akudya cakudya cabwino, cosamalika, cakudya cophikidwa bwino. Mtima wace wokha wakhala nyumba yamapemphero. Amapita kuchalichi kawiri-kawiri ndi mwaulemu nthawi iri yonse ndi kothekera kuli konse angacite. Akonda kupemphera m'cipinda cogonamo pakuti adziwa kuti Mkristu sangathe kukhala ndi moyo ngati sagwirizana ndi Mulungu mwa pemphero.

BUKU LOTSEGUKA lisonyeza kuti Buku Lopatulika ndi buku lotseguka kwa iye, ndipo aliwerenga naliphunzira tsiku ndi tsiku napezamo nzeru ndi mphamvu, moyo ndi kuunika kwabwino, napezanso cuma cosaneneka! Akhala nyali yakumapazi ace ndi lupanga logonjetsera adani ace. Liri mkate wa moyo wa nthawi zonse, madzi ophetsa ludzu lace, kumene asambe ndi kudziyeretsa iye mwini, ndipo lili kalilole m'mene amadziona mwini.

Akonda kunyamula mtanda, pakuti adziwa kuti kulibe mpando wacifumu popanda mtanda. Monga adziwa kuti wauka kwa akufa pamodzi ndi Kristu ku moyo watsopano, afuna-funa zinthu ziri m'mwamba, zinthu zosaoneka ndi maso. Ali wokonzeka kukomana ndi Mulungu ndipo ali ngati mtengo umene wadzalidwa m'mphepete mwa madzi. umene umabala zipatso pa nyengo yace, monga mphanda ya mpesa woonadi, yobala zipatso zambiri. Sadziwa kuopa imfa cifukwa cikondi ceni-ceni ca Mulungu cimene wacilandira mwa Mzimu Woyera cadzaza mtima wace.

Copyright. ANGP

## 10 CITHUNZITHUNZI CAKHUMI




Yesu anati, "Ine ndine kuunika ndi moyo; wokhulupirira Ine, ngakhale amwalira, adzakhala ndi moyo, ndipo yense wakukhala ndi moyo nakhulupirira Ine sadzamwalira nthawi yonse" (Yohane 11 :25-26). "Iye wakumva mau anga ndi kukhulupirira amene ananditumа Ine, ali nao moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wacokera ku imfa nalowa m'moyo" (Yohane 5:24). Mkristu saopa imfa pakuti imfayo yamezedwa m'cigonjetso. Imfawe! Cigonjetso cako ciri kuti? Imfawel Mbola yako iri kuti? Koma ayamikike Mulungu, amene atipatsa ife cigonjetso mwa Ambuye Yesu Kristu ( 1 Akorinto 15:54-57).

Munthu amene amakhala ndi kuyenda ndi Mulungu, saopa za imfa. Pamene nthawi ya imfa ifika, adzapita mokondwera, monga Mtumwi Paulo anena, "Pokhala naco colaka-laka ca kucoka kukhala ndi Kristu, ndiko kwabwino koposa-posatu" (Afilipi 1 :23).

Mkristu afunitsitsa kuona nkhope ya Kristu amene anafera iye ndi kumuombola pa mtanda. Mzimu Woyera umkumbutsanso iye za mau a Yesu Kristu amene ati, "Mtima wanu usabvutike; mukhulupirira Mulungu, khulupirirani Inenso, m'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikudali kutero, ndikadakuuzani inu, pakuti ndipita kukukonzerani inu malo. Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli ineko, mukakhale inuso (Yohane 14:1-4). "Zimene diso silinaziona, ndi khutu silinazimva, nisizinalowa mu mtima wa munthu, zimene ziri zones Mulungu anakonzeratu iwo akumkonda Iye" (1 Akorinto Palibe cinenero cokwanira pa dziko lapansi cimene cingathe 2:9). Kufotokoza za ulemerero wa malo akumwamba okonzedwera iwo amene atsata Ambuye Yesu Kristu pansi pano.

M'malo mwa Woopsyayo, ndiye Imfa, mngelo kapena mthenga wa Mulungu alinkuoneka pa cithunzithunzi com alizaci. Alikudikira kutenga mzimu wa wolungama kwa Mulungu. Moyo ndi mzimu zamasuka ku nsinga za thupi, ndipo zipata zotseguka za Kumwamba zilikumlandira ku cifuwa ca Iye amene moyo wace unamkonda, amene anamkhalira namfera pa dziko lapansi. Cimwemwe cidikira pamaso pa Mulungu kumene adzapatsidwa moni ndi Yehova ndi Mbuye wace ndi mau omuyamikira awa. "Cabwino, kapolo iwe wabwino ndi wokhulupirika; lowa iwe m'cikondwero ca mbuye wako" (Mateyu 25:21 ). Satana alibe mphamvu pa iye konse, pakuti, "Imfa ya okondedwa ace nja mtengo wace pamaso pa Yehova" (Masalmo 116:15). "Ndipo ndinamva mau ocokera Kumwamba ndi kunena,

Copyright ANGP

Lemba, Odala akufa akumwalira mwa Ambuye, kuyambira tsopano; inde; anena Mzimu, kuti akapumule ku zolemetsa zao, pakuti nchito zao zitsatana nao pamodzi" (Cibv. 14:13).

Tamverani owerenga, Mulungu akuthandizeni kupereka mtima wanu kwa iye amene akonda inu, pakuti alikuitana inu tsopano ndi kunena, "Mwana wanga, undipatse mtima wako" (Miyambo 23:26). Patsani Yesu zothodwetsa mtima wanu, kukaika, mtima wakuwawa, ndipo adzakupatsani mtima watsopano ndi mzimu watsopano m'kati mwanu. Musadzinyenge nokha ndi mtima wanu wonyenga kutsata zofuna zace, pakuti, "Wokhulupirira mtima wace ali wopusa; koma woyenda mwa nzeru adzapulumuka" (Miyambo 28:26). Siyani macimo anu ndipo mudziphathikire kucilungamo, "Pakuti mphotho ya ucimo ndi imfa", koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wa mwa Yesu Kristu" (Aroma 6:23).

*Ndipo inu amene mwapatsa moyo wanu kwa Mulungu, "gwiritsani kwambiri mau akumweka, m'cikhulupiriro ndi m'cikondi cimene ciri mwa Yesu". Pa cifukwa comweco Paulo ananena mu 2 Timoteo 1 :12, "Cifukwa ca icico ndinacha zowawa izi; komatu sindicita manyazi pakuti ndimdziwa lye amene ndinakhulupirira, ndipo ndikopeka mtima kuti ali wa mphawu ya kudikira cosungitsa cangaco kufikira tsiku lijalo". Khalani inu mu mzimu wacikhulupiriro. Pempherani mwa Mzimu Woyera! Dzisungeni m'cikondi ca Mulungu, ndipo yang'anani kwa Yesu, Njira, Coonadi ndi Moyo, Ambuye wathu amene adzalandira ace - "Mfumu yamafumu ndi Ambuye wa ambuye".*

*Ndipo kwa lye amene akhoza kukudikirani mungakhumudwe, ndi kukuimikani pamaso pa ulemerero wace opanda cirema m'kukondwera kwa Mulungu yekha, Mpulumutsi, wathu, mwa Yesu Krlstu Ambuye wathu, zlkhale ulemerero, ukuru, mphamvu, ndi ulamuliro zisanayambe nthawi, ndi tsopano, ndikufikira nthawi zonse Ameni' (Yuda 1:24-25).*

*Kuli dziko labwino m'Mwamba,*

*Lakuwala koposa dzuwa,*

*Yesu atikonzera malo*

*Pokhalira ife komweko.*

Chorus

*Bwinoli tipita*

*Tikomana ku dziko lija.*

*Tidzayimba komweko nyimbo*

*Za abwino omvera Yesu,*

*Sitidzamva cisoni ife,*

*Tidzakondwa masiku onse.*

Copyright: ANGP

**A SPECIAL WORD FROM ANGP**

**UN MONDE SPÉCIAL DE L'ANGP**

**UMA PALAVRA ESPECIAL DA ANGP**

**This booklet "The Heart of Man" is available in over 538 languages and dialects spoken throughout the world (Africa, Asia, The Far East, South America, Europe, etc.) Our Heart Book is now also available on cell phones, tablets, etc from www.angp-hb.co.za**

**Le livre du "Coeur de l'homme" peut etre obtenu en plus de 538 langues et dialectes parles dans le monde entier, a savoir: Afrique, Amerique, Asie, Extreme Orient, Europe. Notre Livre du Coeur est maintenant aussi disponible sur votre Telephone cellular, plaques, etc. de www.angp-hb.co.za**

**Este livro "O Coracao do Homem" e obtfdo em mais de 538 linguas e dialectos falados em todo o mundo, a saber: (Africa, Asia, America do Sul, Extremo Oriente, Europa, etc). O nosso Livro O Coração do Homem tambem esta agora disponivel em telefone celular, tablets, etc. de www.angp-hb.co.za**

**The 10 heart pictures contained in this booklet are also available in the form of large coloured picture charts (86 x 61cm) bound together in a set of 10 pictures. These "Heart Charts" can be obtained with European or African features and are particularly suitable to be used in conjunction with the Heart Book for class-teaching, open air evangelization etc. Kindly contact us to ascertain the latest subsidized price of this chart.**

**Les 10 images du coeur qui figurent dans ce livre peuvent etre obtenues en tableaux de couleur, format 86 x 61 cm, avec des physionomies europeennes ou africaines. Ils peuvent etre utilises en meme temps que le livre du coeur pour des classes bibliques, a l'ecole du dimanche ou lors de reunions de plein air. Soyez aimable de nous contacter pour assurer les derniers prix en cours du tableau.**

**As 10 imagens do coracao, contidas neste livro podem ser obtidas num conjunto de 10 imagens em colorido no tamanho de (86 x 61 cm). Estes "Cartazes do Coracao podem ser obtfdos com caracterfsticas Europeias e Africanas e podem ser usados em conjuncao com o mesmo livro em classes de ensino biblico, evangelizacao ou ao ar livre. Agradeciamos que nos contacta- se para confirmacao do ultimo preco dos cartazes.**



Copyright: ANGP

**Kindly write to us if you are able to assist us with further translations of our free Gospel literature, informing us of the language into which you could translate this Gospel literature. Your assistance would be appreciated.**
**If you have found salvation in Christ, or have been otherwise blessed through our Gospel literature, please let us know. We would like to thank God with you, and remember you further in our prayers.**

**Nous vous invitons a nous contacter pour faire des arrangements concernant de nouvelles traductions de notre litterature, nous informant de la langue dans laquelle vous pouvez traduire cette litterature evangelique. Votre aide sera beaucoup appreciee.**

**Si vous avez trouve le salut en Christ ou si vous avez ete beni par notre litterature, nous vous prions de nous le faire savoir. Nous aimerions remercier Dieu avec vous et prier pour vous.**

**Nos vos convidamos a nos contactar, afim de fazer qualquer arranjo concernente a novas traducoes de nossa literatura em outras lfnguas. Vossa assistencia sera muito apreciavel.**

**Se tem encontrado a salvacao em Cristo, ou se tem sido abencoado por intermedio da nossa literatura evangelica, faca o favor de nos informar. Pois nos gostarfamos de agradecer a Deus juntamente convosco, e lembra-lo sempre em nossas oracoes.**

**For free Gospel literature, books and tracts in over 538 languages, write to:**

**Pour obtenir gratuitement de la litterature evangelique, des livres et des traites en plus de 538 langues, ecrivez a:**

**Para obter gratuftamente a literatura evangelica, livros e folhetos em mais de 538 lfnguas diferentes escreva para:**

**ALL NATIONS GOSPEL PUBLISHERS**
**P.O. Box 2191**
**PRETORIA**
**0001**
**R.S.A.**

**A Gospel Literature Mission financed by donations**
**Une Mission de litterature evangelique financee de dons**
**Missao de literatura Evanqelica financiada por donativos**

**(Reg. No. 1961/001798/08)**

**DOWNLOAD BOOKLETS**: www.angp-hb.co.za **ORDER FREE LITERATURE**: info@angp.co.za

Copyright: ANGP